



# Dimba la Keyhole Garden

## Buku la alimi ndi aphunzitsi

## (Chifukwa, Kuti, Chiani,Liti ndipo Motani)








german cooperation
DEUTSCHE ZUSAMMENARBEIT
Implemented by giz Deutsche Gesellschaft für Internationale Zusammenarbeit (GIZ) GmbH
CRS CATHOLIC RELIEF SERVICES

# KODI DIMBA LA KEYHOLE GARDEN NDILOTANI?




Chonde Onetsetsani !



1/3

Madzi ochepa

# Kodi dimba la Keyhole Garden (KHG) ndilotani ?

**Dimba la keyhole garden** ndi mu bed wapamwamba wozungulira womwe ulinso ndi kanjira mopita, ndi swanda yoluka monga mng'oma yoimika pakati mothira zoolera komanso mothirilira madzi.

**Ndi lochedwa** keyhole gadren chifukwa njira mopita ndi swanda pakati pa dimba, zimaoneka ngati m'bowo wa kiyi ukazipenya kuchoka m'mwamba.

## ⊕ Kusebenzensha madzi ang'ono

- ⊕ Silifuna madzi othilirira pafupi pafupi
- ⊕ Limasunga madzi chifukwa cha mapangidwe ache okhala ndi zinyalala
- ⊕ Limasunga mnyontho ndipo limabweretsa nthaka ku dothi kuzera mu zoolera zomwe zimaola.
- ⊕ Zoolera zimapangitsa kuti madzi alowe bwino mbali zonse za dimba
- ⊕ Kuchepa kwa dimba kumateteza madzi kukamukira

# PHINDU LA KEYHOLE GARDEN



## Chonde Onetsetsani !

- Kusebenzesa madzi ang'ono
- Kusebenzesa mphamvu zochepa
- Kudya zamasamba zambiri
- 4+ Kubyala mbeu zinai zosiyana-siyana
- Pafupi ndi  nyumba yanu
- Losadula, losavuta kumanga

# Phindu la Keyhole Garden?

**Dimba la keyhole** garden ndi m'lowa malo weni weni wa dimba lomwe tima lima la chizolowezi, dimba la ku msinje. Keyhole garden ndi chisulo chomwe chingathandize kupititsa patsogolo kudya zakudya zosiyana siyana za masamba chaka chonse


## ⊕ Phindu

- ⊕ Limasunga mnyontho mu nthawi ya m'malanga ndipo **lisebenzesa madzi ang'ono.**
- ⊕ Kusebenzesa mphamvu zochepa-mwaichi, anthu olemara kapena odwalirira mu banja angakwanise kusebenza mu dimbali.


- ⊕ Limabereka ndiyo za **masamba zambiri za thanzi** pa malo ochepa.
- ⊕ Limalola kubyala **mbeu zinai za masamba zosiyana siyana** pa nthawi imodzi, kupititsa patsogolo kadyedwe ka thanzi pa banja.
- ⊕ Silifunika malo akulu – **likhoza kumangidwa pafupi ndi nyumba yanu**.
- ⊕ **Losadula, losavuta** kumanga ndi kusamala.

# KUSANKHA MALO A KEYHOLE GARDEN

## Dimba la Keyhole garden pafupi ndi nyumba



**Chonde Onetsetsani !**



**=Nthambulo imodzi (1 meter)**

# Kusankha Malo a Keyhole Garden

✓ **Dimba la Keyhole garden** lifunika kukhala pafupi ndi nyumba. Malo omangirapo dimba afunika kukhala patali ndi Mthunzi, koma pafupi ndi nyumba kuti kusamala mbeu kukhale kosavuta.

✓ **Malo omangapo keyhole garden** ayenera kukhala akulu kuti alole kumanga mpanda ozungulira dimba kuteteza ziweto ndi mbala.

## ⊕ Malo a dimba afunika kukhala:

- ⊕ **Akulu bwino**
  (nthambulo zinai mkati [4 meters])
- ⊕ **Kopanda zinthu zosokoneza**
  (Miyala zikulu zikulu kapena mitengo siziyenera kupezeka pa malopo kuti pasavute pa nthawi yomanga)
- ⊕ **Pa mtetete**
  (Kulola mbeu kuti zilandire mphamvu ya dzuwa kuti zikule bwino mwa thanzi)

# KUKONZA MALO A KEYHOLE GARDEN


1



2



3




## Chonde Onetsetsani !

**Nthambulo ziwiri (2 meters)**



# Kukonza malo a Keyhole Garden

**Ndondomeko:**




**Konzani** nthambo - nthambulo ziwiri mu utali monga chitenje chimodzi muutali. Pambuyo pake, pimani ndi kulemba pamalo a dimba la keyhole garden kugwiritsa nchito nthambo mwapimayo.



**Limani** ndi kukonza pa malopo.



**Salazani** malowo kuti mukhale ndi chipupa chokhazikika bwino ndiponso kuti mulole madzi ndi zakudya kulowa bwino mdimba lonse la keyhole.



**Pimani** nthambulo imodzi (monga chitenge muufupi) pakati pa chipupa cha dimba kufikila pa mpanda.


# KUMANGA DIMBA LA KEYHOLE GARDEN(I)


## ! Chonde Onetsetsani

**Zinthu zofunika:**


- Nchelwa zokwanira 550 zoshoka, mwina zadothi
- Dothi la pa chulu
- Madzi
- Swanda
- Zida zosebenzesa


1





2







# Kumanga dimba la Keyhole Garden




**Onetsetsani Zomangila**: Nchelwa 550 zoshoka mwina zadothi, Dothi la pa chulu, Madzi, Swanda, Nkhasu, Fosholo, Sando, Mtengo, Piki, nthambo ndi mpimo womangira




**Pimani** nthambo molingana ndi utali wa chitenje (nthambulo ziwiri ). Petekani nthamboyo pakati ndipo mangani mphompho kumathero konse kuwiri. Khomani mphombo imodzi pansi pakati-kati pa malo omwe mwakonza.

**Gwirani** mphompho yosakhomedwa yomangirira ku nthambo ndi kudonsa, ndipo lembani pansi mozungulira.



**Kumbani** maziko yolowa dzanja limozi pansi (30cm) ndi kuyamba kumanga poyalika nchelwa cha m'mimba. Maziko afunika kumangidwa ndi nchelwa zoyalikidwa cham'mimba.





**Pofuna kupima** 30cm, gwiritsani nchito dzanja - kulinganiza utali ochokera kothera kufikira poyambila dzanja la munthu wamkulu.

# KUMANGA DIMBA LA KEYHOLE GARDEN (II)

**! Chonde Onetsetsani Note**

Kugwiritsa nchito dothi lapachulu ndi nchelwa za dothi nizotheka.
Koma nchelwa zoshoka ndi cementi, zipanga dimba la Keyhole garden kukhala lolimba.







# Kumanga dimba la Keyhole Garden


## Ndondomeko



**Mangani** chipupa nthambulo imodzi  mu utali kuchokera pa maziko kusebenzesa dothi la pa chulu losankhaniza ndi madzi.




**Pangani** swanda pogwiritsa nchito tumitengo tukulu-tukulu tokwanira khumi limodzi ndi tuwili (12) toyenzekedwa pansi mozungulira (50—80cm), mwachisanzo mpimo wa manja atatu cham'mimba ndi kumanga mozungulira kusebenzetsa tumitengo tung'ono -tung'ono kufikila nthambulo ndi dzanja imodzi (1.3meters) mu utali.



**Ikani** swanda pakati-kati pa dimba la Keyhole garden pomwe muyamba kuikamo dothi, manyowa ndi zina. Swanda mu dimba limagwiritsidwa nchito yothiramo zinyalala kuti ziwolere ndipo yimathandizanso kuti madzi ndi nthaka zizipita ku mbali zonse za keyhole garden.

# ZIGAWO NDI NTHAKA YA DOTHI MU KEYHOLE GARDEN




**Chonde Onetsetsani !**

## MAPULASITIKI YAYI!



# MAGAWO NDI NTHAKA YA DOTHI MU KEYHOLE GARDEN

✓ **Pambuyo** pomanga dimba la keyhole garden ndi kulola tsiku limodzi kapena awiri kuti liume, lidzadzeni ndi zinthu zofunikira izi:

| | |
|---|---|
| 1. Mayani a nthochi, dolopiyo, gavi | 5. Phulusa la mitengo |
| 2. Zouuma za zomela | 6. Dothi la ma chulu |
| 3. Dothi la pa chulu | 7. Dothi lapa mwamba losakaniza manyowa ndi zoolera |
| 4. Manyowa | |

✓ **Thirani** manyowa ndi zoolera mu dimba pa nthawi yomanga ndi pa nthawi yomwe mukuchita kasintha sintha wa mbeu. Pofuna kusunga nthaka ya dothi, onjezerani manyowa ouma ndi dothi la pa mwamba pamene izi zikubwerera pansi.

✗ Zinthu zopangidwa ndi **Aluminium** kapena **Lead** sizifunika kuikidwa mu key-hole garden chifukwa ziophyeza chilengedwe.

## ⊕ Kuolesa Zinyalala mu Swanda ya Keyhole Garden :

⊕ **Chifukwa nichani kuolesa zinyalala?**
(Zoolera zimapereka zakudya zofunikira pakukula kwa mbeu)

⊕ **Mo'olesera Zinyalala**
(Ikani zinyalala zomwe zimaola mu swanda kuti zipitise patsogolo nthaka ya dothi. Osaika ma pulasitiki mu swanda)

⊕ **Osaikamo manyowa osauma!**
(Pewani kuika manyowa osauma a nyama mu Keyhole graden chifukwa yamatentha mbeu zing'ono zong'ono)

# KUKONZEKERA NDI KUBYALA MBEU MU KEYHOLE GARDEN



## Chonde Onetsetsani !

### ZOYENELA KUBWALA

**Zamasamba zobiriwira kwambiri**
- Spinachi
- Bondwe
- Rape
- Mpilu

**Mbeu za mizyu**
- Carrot
- Beetroot/Mkungu
- Ginger
- Anyenzi

**Mbeu Zina**
- Chinese Kabichi
- Green Beans

# KUKONZEKERA NDI KUBYALA MBEU MU KEYHOLE GARDEN

- **Konzekerani kubyala** njere za mbeu zobvomerezedwa za thanzi, zamasamba mu keyhole garden.
- **Byalani** mbeu zosiyana siyana mu dimba la keyhole garden kuti mupeze phindu la malo anu, nthaka ya dothi komanso kusamaliridwe ka tudoyo.
- **Osalima** mbeu zopitirira zinai za masamba mdimba la keyhole garden pa nthawi imodzi.
- **Mbeu zitamela**, chotsani zina kuti zikhale ndi mpata ololedwa kuti muteteze mbeu kulimbana madzi, zakudya ndi dzuwa.

## ⊕ Mbeu Zamasamba zololedwa:

⊕ **Mbeu zobiliwira kwambiri za masamba**

(Spinachi, Bondwe, Rape, Mpilu, Lettuce)

⊕ **Mbeu za mizyu**


(Carrot, Beetroot/mkungu, Ginger, Anyenzi)

⊕ **Mbeu zina**

(Chinese Kabichi, Green beans, Herbs ndi masipaisi/zonunkhiritsa)

# KASAMALIDWE KA MBEU MU KEYHOLE GARDEN






## Chonde Onetsetsani !

**KUSAMALIRA MBEU KU TUDOYO NDI MATENDA**

- ⊕ **GWIRITSANI NCHITO NJIRA MONGA KASINTHA SINTHA WA MBEU, KULIMIRA MBEU PAMODZI NDI ZOMWE ZIPEWETSA TUDOYO, KULIMA MBEU MOSAKANIZA**
- ⊕ **CHOTSANI UDZU NDI MANJA**
- ⊕ **GWIRITSANI NCHITO ZINTHU ZACHILENGEDWE MONGA:**
  - ⊗ *MPHILIPIRI YOGAYA*
  - ⊗ *MAYANI A PAPAYA*
  - ⊗ *FODYA OGAYA*
  - ⊗ *ANYENZI WOFIIRA*
  - ⊗ *GARLIC OGAYA*
  - ⊗ *MADZI A NEEM/MBULUGAMU*
  - ⊗ *MADZI A MANYOWA YA NG'OMBE*
  - ⊗ *GLIRICIDIA*
  - ⊗ *TEPHROSIA*
  - ⊗ *MADZI A MORINGA*

# KASAMALIDWE KA MBEU MU KEYHOLE GARDEN

## Kuchosa Uzu:

**Chotsani** udzu onse m'dimba la Keyhole garden ndi manja, foloko ya mdimba kapena ka khasu kakang'ono.
Udzu ukhozanso kuponderezedwa pouphimba ndi zinyalala

## Kuthirira madzi:

**Pothirira** madzi, thiraninso madzi mukati mu swanda kuti zinyalala ziole komanso kuti nthaka yipite mu mbali yonse ya keyhole garden.
**Munthawi** yamalanga, thirani zigubu ziwiri kapena zitatu zolemera malita 20 (20 litres) pa tsiku.
**Pewani** kuthilira mbeu ndi madzi amchere, kuikamo zakudya za mchere kapena zinthu zomwe siziola.


## ⊕ Kasamalidwe ka mbeu ku tudoyo ndi matenda:

⊕ **Kusamala ndi chiani?**
Zinthu zosebenzesa: Mphilipiri yogaya, Mayani a papaya, Fodya ogaya, Hanyenzi ofiira, Garlic ogaya, Madzi a Neem/mbulugamu, madzi a manyowa ya ng'ombe, Gliricidia, Tephrosia, Madzi a Moringa kapena, Moringa ogaya

⊕ **Kusamalila motani?**
Mukhoza kusakaniza zinthu ziwiri kapena zitatu zomwe zachulidwa pamwamba ndi kuzisusika m'madzi kwa mphindi makhumi awiri ndi zinai (24hrs) ndipo mutha kupanga madzi yomwe yakwaniritsa kugwebana ndi tuduyo kapena matenda

⊕ **Kugwiritsa nchito mankhwala yachizungu**
Izi nizosaloledwa, chifukwa zimaononga chilengedwe ndipo zipeleka chiophyezo ku anthu maka maka azimai apakati ndi ana ag'ono

# KASAMALIDWE NDI KULUMBISA DIMBA




## Chonde Onetsetsani !


### KULIMBISA CHIPUPA



Nchelwa 550 zoshoka



Mathumba atatu a cement




Maziko omagidwa ndi nchelwa zoikidwa cha m'mimba

# KASAMALIDWE NDI KULIMBISA KEYHOLE GARDEN

- **Pewani** kusamira ku chipupa pa nthawi yothirira ndi yothyola ndiyo, ndipo kulima mbeu za mizyu yaitali m'dimba la keyhole garden.
- **Sungani** malo ozungirira dimba la keyhole garden mwaukhondo, ndipo samalilani mpanda ozungurira dimba kuti muteteze ziweto ndi mbala.
- **Mang'alu** afunika kukonzedwa mwamsanga pogwiritsa nchito cementi kapena dothi la pachulu lonaka kuti muteteze kutayika kwa madzi komanso kugwa kwa chipupa.
- **Nthawi zonse** sinthani swanda ikaonongeka.

## ⊕ Mangani dimba la Keyhole Garden lokhalitsa:

### ⊕ Chifukwa?


Dimba la Keyhole garden lomangidwa ndi nchelwa za dothi likhoza kugwa patapita nthawi, koma dimba la keyhole garden lomangidwa ndi nchelwa zoshoka ndi cement limalimba ku mvula ndipo likhala nthawi yaitali.

### ⊕ Likhala nthawi yaitali motani?

Pomanga dimba la keyhole garden lokhalitsa nthawi yaitali, gwiritsani nchito zinthu izi:

- ⊗ Nchelwa zoshoka zili 550
- ⊗ Mathumba atatu a Cement
- ⊗ Maziko yolimba, yolowa pansi yomangidwa ndi nchelwa cha m'mimba

# Dimba la Keyhole Garden




KUDYA ZATHANZI

KUDYA ZAMAGULU OSIYANA-SIYANA

KUDYA ZOSIYANA-SIYANA

MAGULU AZAKUDYA

## Buku la Alimi ndi Aphunzitsi

## (Chifukwa, Kuti, Chiani, Liti ndipo Motani)

**Lotsindikizidwa ndi:**

Unduna wa Zaulimi

Mulungushi House, Independence Ave.
P.O. BOX 50197, Lusaka
Website: www.agriculture.gov.zm
Email: info@agriculture.gov.zm
Lamiya: +260 01-253933

© Malemba ndi Zithunzi-thunzi 2019 Unduna wa Zaulimi
Kujambila kapena kulembanso zili mubukuli mobwereza, kwathunthu kapena pang'ono chabe kuyenera kuchula mutu wa bukuli ndi kupereka ulemu kwa wolemba bukuli pokhala mwini wache.

**Bukuli linalembedwa ndi chithandizo chochokela ku:**

Food and Nutrition Security, Enhanced Resilience Project (FANSER)
Deutsche Gesellschaft für Internationale Zusammenarbeit (GIZ) GmbH
No. 5, Chaholi Road, Rhodes Park
Private Bag RW 37X
Lusaka, Zambia

Moimilila mbali ya:
Federal Ministry for Economic Cooperation and Development (BMZ) Germany